Kora Anaukira Mose ndi Aroni

NUMERI CHAPUTALA 16-17

Sankhani zimene mukuona kuti n’zogwirizana ndi ana anu. Mukambirane zinthuzo monga banja.

WERENGANI NUMERI CHAPUTALA 16-17

Kenako onani zithunzi zofotokoza nkhani ya m’Baibulo (pa Intaneti kapena papepala limene mwasindikiza), ndiyeno kambiranani mafunso amene ali kumapeto.

ZINTHU ZINA ZIMENE MUNGASINDIKIZE



ZITHUNZI

KONGOLETSANI NDI CHEKENI: Werengani Ekisodo 28:15-21. Kenako thandizani ana anu kuti akongoletse miyala yapadera yomwe inkakhala pa chovala pachifuwa. Mukatero, athandizeni kudula chovala pachifuwacho ndipo muwaveke.



ZOTI MUCHITE POPHUNZIRA

MALIZITSANI: Uzani mwana wamng’ono kuti adule chidutswa chokonzera msasa wa Aisiraeli, kenako akonze msasawo. Muuzeninso kuti adule zithunzi za anthu a m’Baibulo omwe atchulidwa m’nkhaniyi. Akachita zimenezi, alembe dzina lake komanso ajambule chithunzi chake pachidutswa china cha munthu chopanda kanthu. Kenako uzani ana anu onse kuti agwiritse ntchito zidutswazo pomalizitsa kukonza msasa wa Aisiraeli komanso poyerekezera zimene Kora anachita. Pagawo lililonse la nkhaniyi, muzifunsa mwana wanu aliyense kuti: “Iweyo ukanakhalapo pa nthawiyi, kodi ukanaima pati?”

SUNGANI KUTI MUZIKUMBUKIRA

KHADI LA MUNTHU WOTCHULIDWA M’BAIBULO: Onani kuti munthuyo anali ndani. Funsani mafunso amene ali pakhadilo. Pogwiritsa ntchito khadili komanso makadi ena amene ali pa jw.org, thandizani ana anu kupeza mayina a anthu ena 5 otchulidwa m’Baibulo amene anali a fuko la Levi: (1) mneneri amene anayamba kutumikira kuchihema ali kamnyamata, (2) ana atatu a Amuramu, ndiponso (3) mwana wa wansembe amene analemba mabuku 4 a m’Baibulo.—**ZOKUTHANDIZANI:** Werengani 1 Samueli 3:1; 1 Mbiri 6:1-3, 33, 34; Yeremiya 1:1.

Mayankho: 1. Samueli. 2. Aroni, Mose, Miriamu. 3. Yeremiya.

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania